


M'busa Tony Alamo | Fuko La Chikhristu La Alamo | Volume 17500

# MAGARETA A MOTO

**Yolembedwa ndi Tony Alamo**

Anthu akaona liwu loti "gareta," amaganiza kuti lili ndi tanthauzo limodzi lokha, "chokoka-bulu, ngolo ya matayala-awiri yogwiritsidwa ntchito m'masiku akale pa nkhondo, mpikisano, ndi zina zambiri," *Webster Dictionary* imanenanso "ona GALIMOTO." Tikayang'ana m'mwamba "galimoto," tikuona liwu likuchokera ku chiyankhulo cha Latin "carrus," kutanthauza "gareta." Gareta limatanthauzanso "(1) galimoto iliyonse pa matayala; (2) galimoto yoyenda pa njanji, monga galimoto ya pamseu, kapena ngolo; (3) galimoto; ndi (4) ndi khola la chikepi kapena kuti eleveta." Tanthauzo lamakono ndikuphatikizapo ndege, maUFO, mbale zowuluka, ndi chonyamulira anthu chili chonse, angelo, ndi zina zambiri. Kumasulira kwa m'chiHeberi kwa "gareta" kungakhale "makamu" kapena "ngolo." Choncho liwu lokuti "gareta" lili ndi matanthauzo ambiri.



*M'busa Alamo ndi malemu mkazi wake Susan pa porogaramu yawo yapa kanema ya dziko lonse, yomwe inajambulidwa ku Grand Ole Opry, Nashville, Tennessee* *Chithunzi chinatengedwa 1975*

Mu 2 Mafumu 6:15, pamene wantchito (kapena mtumiki) wa munthu wa MULUNGU (Elisa) anadzuka msanga m'mawa ndi kupita kunja, anaona khamu pamodzi ndi akavalo ndi magareta ozungulira mzinda (awa sanali magareta a moto, chifukwa ananyamula amuna okha). Wantchito (mtumiki) wa Elisa anamufunsa kuti: "Mphunzitsi, tichite chiyani?" "Usaope," iye anayankha, "Pali ambiri kumbali yathu kuposa mbali yawo." Pamenepo Elisa anapemphera kwa MULUNGU, nati, "AMBUYE, tsegulani maso ake ndipo mupenyetseni." "Ndipo AMBUYE anatsegula maso a mtumiki ndipo anaona mapiri onse atazungulira Elisa atakutidwa ndi akavalo ndi magareta a moto." Magareta awa akusiyana koposa magareta a Asiriya chifukwa magareta awa ananyamula angelo. Iwo ndi "magareta a moto," ndipo saoneka ndi maso a munthu pokhapokha ngati MULUNGU angationetse. IYE akulola anthu ambiri kuona mbale zouluka za Kumwamba lero. Izo zikuyeza dziko lapansi YESU asanabwerenso ku dziko lapansi kachiwiri, ndipo izo zili, monga mwa malangizo a MULUNGU, kuchititsa -tsoka apa ndi apo padziko lapansi chifukwa cha anthu a mwano, kupembedza mafano, ndi njira zina zambiri zoipa.[1]

Anthu ena amakhulupirira kuti chokhacho choyenera kuchita ndi kukhulupirira mawu oti "YESU KHRISTU" ndipo tidzapulumuka. Kwenikweni, chimene MULUNGU akutanthauza ndichakuti tiyenera kukhulupirira zonse zimene AMBUYE wathu YESU ananena, anachita, ndiponso zimene akuchitabe kudzera ku THUPI LAKE, limene liri Mpingo WAKE, Mkwatibwi WAKE. Ichi ndi chifukwa chake IYE amatiuza m'bukhu la Chivumbulutso kuti tiyenera kukhala wotanganidwa mwakhama pakumutsatira IYE.[2]

Anthu ambiri amalengeza kuti amakhulupilira dzina LAKE, monga mdierekezi akhulupiliranso dzina LAKE, ndi kunjenjemera (Yakobo 2:19). Komabe, YESU amatiuza kuti IYE amafuna ife tim'tsatire IYE ndi kusunga malamulo AKE onse, mwa changu![3] Ngati tiswa ngakhale limodzi mwa malamulo AKE, ndi chimodzimodzi kuswa onse, chifukwa ngati tiswa ngakhale limodzi mwa malamulo AKE, ndi kokwanira kutumiza miyoyo yathu ku Gahena wosatha ndi muyaya m'Nyanja ya Moto.[4] Ichi ndi chifukwa chake YESU akutichenjeza kuti IYE sakuchita ntchedzera. IYE anati, "Ine ndidziwa ntchito zako [IYE amadziwa chili chonse chimene ife tikunena ndip-

*(Yapitirira patsamba 2)*

**1** Gen. 19:1-25, Num. 22:1-35, 25:1-9, 2 Sam. 24:1-17, 2 Mafumu 19:35, 1 Mbiri 21:9-30, 2 Mbiri 32:19-22, Chiv. 7:1-2, chap. 8, 9:1-5, 13-21, 14:8-11, 15-20, chap. 16, 18:1-2, 21, 19:17-21, 20:1-3, 21:9 **2** Mat. 3:7-10, 7:13-23, Yoh. 14:12, 15, 21-24, 15:1-14, Aro. 12:5-21, Gal. 5:14-26, Aef. 4:20-32, Tito 2:11-15, Aheb. 2:1-3, Yako. 1:21-27, 1 Pet. 4:7-8, 2 Pet. 1:3-11, 1 Yoh. 2:3-11, 15-17, 3:4-12, Chiv. 3:14-22 **3** Chiv. 3:14-22 **4** Yako. 2:10-11

# MAGARETA A MOTO

*(Yachokera patsamba 1)*

onso kuchita], kuti suli wozizira kapena wotentha: bwezi utakhala wozizira kapena wotentha. Kotero ndiye chifukwa iwe uli wofunda, ndipo osati wozizira kapena wotentha, Ndidzakulavula iwe kuchoka m'kamwa MWANGA" (Chivumbulutso 3:15-16).

Bwanji YEHOVA amadziwa zonse zimene timanena ndiponso kuchita? Tikudziwa kuti zonse zimene tanena ndiponso kuchita, kapena tidzanena ndiponso tidzachita, zinalembedwa m'bukhu.[5] Tikudziwa kuti MULUNGU ali paliponse, ndikuti m›chilengedwe chonse sangakwanemo IYE.[6] IYE alinso ndi mphamvu zonse, kutanthauza IYE ali ndi mphamvu zopanda malire ndi ulamuliro. IYE ndi wamphamvu-zonse.[7] IYE amakhala pali ponse, kutanthauza kupezeka m'malo onse pa nthawi imodzi.[8] Sikanthu MULUNGU kudziwa zonse zimene timanena ndiponso kuchita, ndipo n'zosatheka kuti IYE aname (Ahebri 6:18).

Ndi zofunika kwambiri kuti tikhulupirire YESU pamene IYE akuti tidzaweruzidwa ife chifukwa cha liwu lili lonse lopanda pake.[9] Mateyu 12:36 akuti, "Koma Ine ndinena kwa inu, Kuti liwu lili lonse lopanda pake limene munthu adzalankhula, adzamuwerenga mlandu wake tsiku la chiweruzo." Chivumbulutso 20:11-12 akuti, "Ndipo ndinaona mpando wachifumu waukulu woyera, ndi IYE wakukhalapo, amene nkhope YAKE dziko lapansi ndi kumwamba zinathawa; ndipo sadapezeke malo awo. Ndipo ndinaona akufa, ang'ono ndi akulu, ataima pamaso pa MULUNGU; ndipo mabuku anatsegulidwa: ndipo bukhu lina linatsegulidwa, limene lili bukhu la moyo: ndipo akufa anaweruzidwa mwa zinthu zimene zinalembedwa mu mabuku, monga mwa ntchito zawo."

Ndalemba m'chidutswa china cha zolemba kuti MULUNGU anatumiza angelo AKE kukaononga ochimwa ndi malo ochimwira padziko lapansi.[10] Bukhu la Chivumbulutso limanena za magulu a miliri isanu ndi iwiri yoyamba ndi yachiwiri kuti angelo adzatsanulira mu chiwonongeko cha dziko lapansi lonse lochimwa kwambiri (Chibvumbulutso 8:6 mpaka 9:21, 11:14-19, 16:1-21).

Mngelonso m'modzi anawononga asilikali a Senakeribu, amuna 185,000, mu usiku umodzi wokha. "Ndipo zinachitika usiku umenewo, kuti mngelo wa YEHOVA anapita, ndi kukakantha [kupha] Asuri 185,000 mumsasa wawo: ndipo atadzuka m'mawa kwambiri, onani, onse anali mitembo yakufa" (2 Mafumu 19:35).[11] Pamene Davide anachimwa pakuwerengera Israeli, zimene MULUNGU sanafune kuti achite, MULUNGU anatumiza mngelo m'modzi kukayika mliri pa ana a Israeli, umene anapha 70,000 a iwo (2 Samueli 24:15).

MULUNGU, pokhala paliponse, malo ali wonse nthawi yomweyo, amatumiza angelo AKE, amene ali ndodo YAKE, kutemberera anthu padziko lapansi, kubweretsa chiononongeko kwa ochimwa. Angelo ndi atumikinso amene anatumizidwa kubweretsa mauthenga a chimwemwe kwa anthu monga Mariya ndi Elizabeth.[12]

Tsopano, pali moto ochokera kwa MULUNGU walawilawi umene Mtumwi Petro akunena pa 2 Petro 3:7-14: "Koma kumwamba ndi dziko lapansi, zimene zilipo pano, ndi MAWU womwewo zayikika, kusungira tsiku la chiweruzo ndi chiwonongeko cha anthu osapembedza. Koma, wokondedwa, musayiwale ichi chimodzi, kuti tsiku limodzi likhala kwa Ambuye ngati zaka chikwi, ndi zaka chikwi ngati tsiku limodzi. [Izi zikungotanthauza kuti MULUNGU sakuyenera kukhala pachangu kuweruza inu ndi ine chifukwa moyo wathu ndi waufupi kwambiri.[13] MULUNGU ndi wamuyaya; IYE ndi wamoyo wosatha.14 IYE adziwa kuti inu ndi ine tidzaima pamaso PAKE mukuphethira kumodzi kapena kuwiri kwa diso.[15] IYE ali ndi nthawi yambiri. Pamene nthawi yatha, IYE adzaona inu ndi ine—posachedwapa]. AMBUYE sazengereza lonjezo LAKE [chiweruzo CHAKE], monga ena achiyesa chizengerezo; komatu aleza mtima kwa ife, wosafuna kuti ena awonongeke, koma kuti onse afike ku kulapa [kuphethira maso kawiri kusanathe kwa ziweruzo zathu].

"Koma tsiku la AMBUYE lidzadza ngati mbala mu usiku; m'mene kumwamba kudzapita ndi chiphokoso chachikuru, ndipo zam'mwamba zidzakanganuka ndi kutentha kwakukuru, ndiponso dziko lapansi ndi ntchito zili momwemo zidzatenthedwa. Popeza izi zonse zidzakanganuka kotero, muyenera inu kukhala anthu otani nanga m'malankhulidwe opatulika ndi mu Chipembedzo, Akuyembekezera ndi kufulumira kwa kudza kwake kwa tsiku la MULUNGU, m'menemo m'mwamba pakutentha ndi moto mudzakanganuka, ndipo zam'mwamba zidzasungunuka ndi kutentha kwakukulu? Komabe ife, monga mwa lonjezano LAKE, tiyembekezera kumwamba kwatsopano ndi dziko lapansi latsopano, m'menemo mukhalitsa chilungamo. Momwemo, okondedwa, popeza muyembekeza izi, chitani changu kuti mupezedwe ndi IYE mumtendere, opanda banga ndi opanda chilema."

Pali moto wa MULUNGU umene sumatentha ngati moto tatchula m'mwambawu, umene umatentha kumwamba ndi dziko lapansi lonse. Pano pali zitsanzo zina za moto wa mtundu umenewu. Chivumbulutso 1:13-14 amanena kuti panali m'modzi pakati pa zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri, chizindikiro cha mipingo isanu ndi iwiri, "wonga MWANA wa MUNTHU [YESU], atavala chovala chofikira ku mapazi, ndipo atamangira pachifuwa ndi lamba wa golidi. Mutu WAKE ndi tsitsi LAKE zinali zoyera ngati ubweya, woyera ngati chipale chofewa [fanizo LAKE kukhala MWANA wa NKHOSA wa MULUNGU, anaphedwa asanaikidwe maziko a dziko chifukwa cha machimo a anthu onse amene adzalape[16]]; ndipo maso AKE anali ngati LAWI LA MOTO …."

"Ndipo mngelo wa YEHOVA anaonekera kwa iye [Mose] m'lawi la moto kuchokera pakati pa chitsamba: ndipo iye anayang'ana, ndipo, taonani, chitsamba chinayaka moto, ndipo chitsamba sichinapse" (Eksodo 3:2).

"Ndipo YEHOVA anapita patsogolo pawo [mtundu wa Israeli] usana mu mza-

---

**5** Deut. 31:21, 1 Maf. 8:39, 2 Maf. 19:27, 1 Mbi. 28:9, Yobu 31:4, 34:21-22, 25, Mas. 44:21, 69:5, 139:1-16, 23-24, Yes. 29:15-16, Ezek. 11:5, Luka 16:15, Mach. 15:18, Aheb. 4:13, 1 Yoh. 3:20, Chiv. 20:12-13 **6** 1 Mafu. 8:27, 2 Mbiri. 2:6, Mas. 139:7-16, Miy. 15:3, 11, Yer. 23:23-24 **7** Gen. 17:1, 35:11-12, 1 Mbiri. 29:11-12, 2 Mbiri 20:6, Yobu 42:2, Mas. 104:1-32, Yes. 26:4, 40:12-18, 21-28, Mat. 19:26, 24:30, 28:18, Luka 1:37, Yoh. 17:2, Mach. 26:8, Aef. 1:19-22, Akol. 1:12-19, 2:10, Aheb. 1:1-12, Chiv. 4:11, 16:9, 19:6 **8** Mas. 139:3-10, Yer. 23:23-24, Mach. 7:48-49, 17:24 **9** Mas. 19:14, Mat. 12:36-37 **10** "Asilikali Ankhondo Yapamtunda Ndi Mlengalenga A Mulungu (Alonda)," "Angelo a Kumwamba Kuyandama Pamodzi Mlengalenga Pamwamba Pa Planeti Yathu," Gen. 19:1-25, Eks. 33:1-3, 2 Sam. chap. 24, 2 Maf. 6:8-17, 19:1-35, 2 Mbiri. 20:1-24, 32:1-22, Mas. 34:7, 35:4-6, Zek. 1:7-21, Mat. 13:36-43, 47-50, 16:27, Mach. 12:21-23, Yuda 14-15, Chiv. 7:1-2, chap. 8, 9:1-5, 12-21, 14:8-11, 15-20, 15:1, chap. 16, 18:1-2, 21, 19:17-21, 20:1-3, 21:9 **11** 2 Mbiri. 32:19-21, Yes. 37:36 **12** Gen. 16:6-15, 21:14-21, Ower. chap. 13, 1 Maf. 19:1-8, Dan. chap. 6, Mat. 1:18-25, 28:1-8, Luka 1:5-20, 26-38, 2:7-16, Mach. 1:9-11, 10:3-6, 12:1-11, 27:9-44 **13** 1 Mbiri 29:15, Yobu 4:17-21, 7:6-10, 9:25-26, Mas. 22:29, 39:4-6, Yes. 2:22, 40:6-7, Yako. 1:10-11, 4:14, 1 Pet. 1:24 **14** Eks. 15:18, Deut. 32:39-40, Yobu 36:26, Mas. 9:7, 10:16, 29:10, 45:6, 90:1-4, 93:2, 102:12, 24-27, 146:10, Yes. 44:6, Maliro 5:19, Dan. 4:34, Luka 1:33, Aheb. 1:10-12, 1 Tim. 1:17, 6:15-16, Chiv. 1:8, 17-18, 4:8-11 **15** Mas. 73:18-19, Mlal. 12:13-14, Dan. 7:9-10, Mach. 17:30-31, Aroma. 2:5-13, 16, 14:10-12, 1 Akor. 15:52, 2 Akor. 5:10, Aheb. 10:26-31, Chiv. 11:18, 20:11-15 **16** Yes. 53:4-12, Yoh. 1:29, 1 Pet. 1:18-19, Chiv. chap. 5, 6:16, 7:9-17, 12:11, 13:8, 14:1-4, 15:3, 17:14, 19:7-9, 21:9-27

ti wa mtambo, nawatsogolera njira; ndipo usiku mu mzati wa moto, nawapatsa kuunika; kuti ayende usana ndi usiku" (Eksodo 13:21).

"Ndipo maonekedwe a ulemerero wa YEHOVA anali ngati moto wonyeketsa pamwamba pa phiri pamaso pa ana a Israeli" (Eksodo 24:17).

Mu Mateyu 3:11, Yohane M'batizi akuti, "Inetu ndikubatizani inu ndi madzi kuloza ku kutembenuka mtima: koma IYE [YESU] amene akudza pambuyo panga ndi wamphamvu kuposa ine, nsapato zake ine sindili woyenera kunyamula: IYE adzakubatizani inu ndi MZIMU WOYERA, ndiponso ndi MOTO."

"Ndipo kunali, pamene IYE [YESU] anakhala nawo pachakudya, IYE anatenga mkate, naudalitsa, naunyema, napatsa iwo. Ndipo maso awo anatseguka, ndipo anam'zindikira IYE; ndipo IYE anasowa pamaso pawo. Ndipo anati wina ndi mzake, Kodi mtima wathu sunatenthe mkati mwathu, pamene IYE anayankhula nafe m'njira, ndi pamene IYE anatitsegulira malembo?" (Luka 24:30-32).

Mu 2 Mafumu 6:17, Elisa anapemphera kwa MULUNGU kuti atsegule maso a mtumiki wake, wantchito wake, "Tsegulani maso ake, kuti aone. Ndipo YEHOVA anatsegula maso a mnyamatayo; ndipo anaona: ndipo, taonani, phiri linadzadza ndi mahatchi ndi magareta [ngolo, maUFO, mbale zowuluka] a MOTO [chimodzimodzi ndi MZIMU WOYERA, MOTO umene YESU amabatizira pamene tadzadzidwa ndi mphamvu yochokera kumwamba, kubatizidwa ndi MZIMU WOYERA ndi MOTO] mozungulira Elisa."

Mu Machitidwe 1:7-9, YESU anati kwa ophunzira AKE, "Sikuli kwa inu kudziwa nthawi kapena nyengo, zimene ATATE anayika mu ulamuliro WAKE yekha. Koma mudzalandira mphamvu [MOTO ndi KUDZIPEREKA], pamene MZIMU WOYERA atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni ZANGA m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya monse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero a dziko lapansi. Ndipo m'mene ananena izi, pamene iwo ali chipenyerere, IYE ananyamulidwa; ndipo mtambo unamlandira IYE kum'chotsa pamaso pawo."




MZIMU WOYERA unatenga YESU kupita KUMWAMBA. Ndi MZIMU WOYERA umene ukuyendetsa maUFO, mbale zowuluka kapena magareta a MOTO amene ali ndi angelo mwa iwo. Iwo siochokera ku pulaneti iliyonse. Iwo ndi a Kumwamba—ochokera Kumwamba—kufufuza dziko lapansi patatsala pang'ono kutha kwa nthawi, YESU asanabwerenso padziko lapansi. Iwonso akukwaniritsa kukhanzikitsa chiyambi cha zowawa zimene YESU ananena mu mutu wa 24 wa Mateyu. Awa ndi mawu a YESU: "Yang'anirani asasokeretse inu munthu. Pakuti ambiri adzadza m'dzina LANGA, nadzanena, Ine ndine KHRISTU; nadzasokeretsa anthu ambiri. Ndipo inu mudzayamba kumva za nkhondo ndi mbiri za nkhondo: onani kuti musadere nkhawa: pakuti ziyenera izi kuchitika, koma chitsiriziro sichinafike. Pakuti mtundu wa anthu udzawukirana ndi mtundu wina, ndipo ufumu kuukirana ndi ufumu wina: ndipo kudzakhala njala, ndi miliri [mliri ndi nthenda yobuka yowopsa; zakuvutitsa; chili chonse chimene mungaganizire kuti n'choopsa], ndi zivomezi m'malo osiyanasiyana. Zonsezi ndicho chiyambi cha zowawa" (Mateyu 24:4-8).

Kodi inu simukuganiza kuti ife tapitilira chiyambi cha zowawa? Vesi 9 ikuti, "Ndiye iwo adzakuperekani inu ku chisautso [ndipo MULUNGU ndi angelo akuona!], nadzakuphani inu [monga anapha amuna, akazi, ndi ana pa Waco mwa nkhanza—ndipo MULUNGU ndi angelo AKE akuona. Janet Reno ndi Bill Clinton ananena pa national TV ya dziko kuti onse avomereza izi kwathunthu. Bill Clinton anati, 'Izi ziphunzitse anthu kuti asamatenge mbali mu miyambo ya upandu.' Uwu unali mchitidwe wophwanya malamulo, wotsutsana ndi Kukonza Koyamba (First Amendment) kumene Bill Clinton anachita—ndipo anati iye anachita.]: Ndipo inu [Akhristu oona] mudzadedwa ndi mafuko onse chifukwa cha dzina LANGA [chifukwa mum'konda YESU. YESU ndi oyang'anira akuona zonse zimene zikuchitika pano.]. Ndiyeno anthu ambiri adzapunthwa [chifukwa cha chizunzo chimene chimabwera chifukwa cha kukhala m'Khristu woona (osati Katolika)], ndipo adzaperekana wina ndi mzake [monga anachitira], ndipo adzadana wina ndi mzake [monga akuchitira]. Ndipo aneneri wonama ambiri [ochokera kwa Satana] adzawuka, nadzasokeretsa anthu ambiri. [Chivumbulutso 12:9 amati 'Ndipo chidaponyedwa pansi chinjoka chachikulu, njoka yokalambayo, yotchedwa mdierekezi, ndiponso Satana, amene adanyenga dziko lonse lapansi: iye anaponyedwa kunja (kuchokera Kumwamba) kupita kudziko lapansi, ndipo angelo ake anaponyedwa kunja pamodzi naye.'] Ndipo chifukwa cha kuchuluka kwa kusaweruzika, chikondano cha anthu aunyinji chidzazilala. Koma iye opilira kufikira chimaliziro, yemweyo adzapulumutsidwa. [MULUNGU ndi magareta a MOTO akuona ndi kumva zonse.] Ndipo Uthenga wabwinowu [zoonadi izi] wa ufumu umene udzalalikidwa padziko lonse lapansi ukhale umboni ku mitundu yonse; ndipo pomwepo chimaliziro [cha dziko] chidzafika. Pamene mudzawona chonyansa cha kupululutsa, chimene chi-

*(Yapitirira patsamba 4)*

## Ghana

Wokondedwa M'busa Tony Alamo,

Mulungu akudalitseni kopambana chifukwa cha ntchito zanu zabwino zimene mukuchitabe ku mitundu yonse. Mpingo wanga, The Grace Hour Ministry International, Ghana, unapita ku mizinda ina yozungulira Mafi-Kumasi kukagawa nkhani zam'makalata za Tony Alamo kwa anthu oposa 5,000. Uthenga wabwino tinawabweretsera iwo, ndipo anthu 500 anadzipereka kwa Khristu ndipo tinagwirizana kuti tizisonkhana Lachiwiri ndi Lamlungu lili lonse musabata kudzaphunzira Mawu a Mulungu, ndi kupempherera utumiki wa Tony Alamo. Mutu wa nkhani wa chaka kwa iwo ndi: 2013 Chaka Chopatulika Chopambana (1 Mafumu 8:56). Ine monga mtsogoleri wa gulu, ndafuna kugwiritsa ntchito mwayi umenewu wopempha zolemba zanu 20,000, Mabaibulo 50 a atsogoleri atsopano a gululi, ndi makope 300 a mabuku a *Mesiya* odzagwiritsa ntchito pa msonkhano wa panja (Crusade) wachipembedzo umene ukubwera pa 11–20 February 2013, ndiponso kupempherera kuti Mulungu amve mapemphero athu ndi kupulumutsa M'busa Alamo m'ndende.

Stephen Kwabla Gbeve — Volta Region, Ghana

## MAGARETA A MOTO

*(Yachokera patsamba 3)*

danenedwa ndi Danieli mneneri, chitaima m'malo oyera (amene awerenga, amvetsetse:)" (Mateyu 24:9-15).

Chonyansa chimene chimapangitsa dziko lonse kukhala bwinja ndi pamene Papa ku Rome, Vatican, asonkhanitsa atsogoleri a mafuko onse pamodzi kuti apange One World Government, New World Order, imene ili chirombo. Izi zimachitika ndi mzimu wa Satana.

Pano pali nkhani yapa 10 December, 2012 yokhudzana ndi nkhani yam'nyuzipepala yochokera ku Vatican: "Vatican Calls for World Government and New World Order," ndi Andrew Puhanic, mthandizi (contributor), Activist Post. "Mtsogoleri wa Mpingo waupandu wa Katolika [cult], Papa Benedict XVI, waitanitsa kuti kukhazikitsidwe World Government ndi New World Order. M'zolankhula zimene zinanenedwa ku Pontifical Council for Justice and Peace Lolemba, 3 December, 2012, Papa anaitanitsa za 'kumangidwa kwa mudzi wa dziko lonse (world community), ndi ulamuliro olingana,' kutumikira 'zokomera aliyense wa banja la munthu.'"

Zokomera aliyense? Mu Chivumbulutso 16:1-2, MULUNGU anati kuti ngati tilowa bungwe lathemberero ngati ili monga chirombo ichi, One World Government iyi, New World Order iyi, ndiye kuti tikumata tsoka lathu lomwe: "Ndipo ndinamva mawu akulu ku kachisi akunena kwa angelo asanu ndi awiri, Mukani njira zanu, ndipo tsanulirani mbale za mkwiyo wa MULUNGU pa dziko lapansi. Ndipo woyamba anachoka, natsanulira mbale yake pa dziko lapansi; ndipo kunakhala chilonda choipa ndi chosautsa pa anthu amene anali ndi chizindikiro cha chirombo [chimenenso chili chizindikiro cha One World Government, New World Order], ndi pa iwo wolambira fano lake [limene lili dziko lonse la anthu wonyengedwa, wosapulumutsidwa]."

Chivumbulutso 19:20 amati, "Ndipo chirombo [One World Government, New World Order yotsogoleredwa ndi Rome[17]] chinatengedwa, ndi pamodzi nacho m'neneri wonyenga [amene ndi mwambo wa mpingo wa Roma Katolika] wakuchita zozizwitsa [zozizwitsa zonyenga, monga maonekedwe a Mariya, ndi zifaniziro za YESU akukhetsa mwazi pa mtanda, ndi mafano a Mariya manja ake akukhetsa mwazi] pamaso pake, zimene anasokeretsa nazo iwo amene analandira lemba la chirombo [dziko lonse la anthu amene Satana anawanyenga], ndi iwo akulambira fano lake [amene anatumikira boma lake, ndipo iye amawalipira]. Iwo awiri anaponyedwa ali ndi moyo m'nyanja yamoto yakutentha ndi sulfure."

Izi zimene papa akuchita ndi kulankhula zikupangitsa mwachangu dziko lonyengedwa kuti litenge chilemba cha chirombo pa dzanja lawo kapena pamphumi. Onse akutenga chilemba ichi ali chimodzimodzi ndi kuchitira mwano MZIMU WOYERA, ndipo papa uyu akunyenga ambiri m'dzina la mtendere ndi chitetezo.[18] Chivumbulutso 13:16-17 akuti, "Ndipo iye [Satana m'thupi la papa, mpingo wake wabodza, ndi New World Order, One World Government yake] apangitsa kuti onse, ang'ono ndi akulu, olemera ndi osauka, mfulu ndi akapolo, alandire chilembo pa dzanja lawo lamanja, kapena pamphumi pawo: Ndi kuti munthu sangakhoze kugula kapena kugulitsa, koma iye yekha wakukhala nacho chilembo, kapena dzina la chirombo, kapena chiwerengero cha dzina lake."

Mu zosindikiza zake, Papa ananenanso kuti iyi ndi, "njira kutetezera mtendere

**17** Chiv. 17:1-9, 15-18, 18:1-10, 15-19, 24, 19:1-3 **18** Yer. 6:13-14, 8:11, Ezek. 13:9-10, Mat. 10:34, 1 Atesa. 5:1-9

## California

Mpingo wa Alamo,

Zikomo chifukwa cha bokosi lotsiriza la mabuku. Nditha kugwiritsa ntchito bokosi lina. Ndatsala ndi mabokosi atatu okha a mabuku!

Ndikaona magalimoto ambiri ndikuyenera kuwaika pa galasi la kutsogolo la galimoto (windshield)! Tepi ya M'busa Alamo ya kufesa mbewu inandikhudza kwambiri pa moyo wanga. M'busa Tony ananenanso, "Chitani china chake pamene mungathe." Dzulo ndinaona sukulu ya mpingo wa Lutheran ili ndi magalimoto ambiri komanso koleji, kenako dera la doko la Seal Beach ndipo mabuku anandithera! Linali tsiku lalikulu mwa Ambuye ndipo ndinasangalaladi ndi masewera anga omwe ndimawakonda, "kumenya mbuyo ya mdierekezi," ndipo, monga M'busa Tony ananenera, "zimandipatsa chimwemwe chachikulu." Anthu ambiri amamva za Tony kudzera mwa aulutsi olamuliridwa ndi Vatican monga mukudziwa! Pamene ndapereka mabuku kwa anthu awa, ndimaonetsetsa kuti amve chilungamo chenicheni cha M'busa Alamo! Makampeni amene amamuchitira iye ndiabodza kwathunthu ndipo amadana naye (monga anachitira ndi Yesu) chifukwa ndi mdani woyamba wa aliyense chifukwa chowawulutsa a Vatican, gulu la uSatana. Ndi nkhondo ya mawu, monga M'busa Alamo ananena, choonadi cha Mulungu kutsutsana ndi mabodza a Satana! Koma anthu ambiri amene ndinawapatsa mabuku akumvera kwa choonadi chenicheni cha utumiki wa Alamo! Pamene akuonjezera kuzunza Tony, ndipamene ine ndikuonjezera kudziwa kuti iye ali wa Ambuye. Chomwe mukuyenera kuchita ndi kumvera mauthenga kuti mudziwe iye ndi mneneri wa Mulungu! Mphotho yanu ndi yaikulu Kumwamba, M'busa Tony, kupereka moyo wanu kwa Mulungu kuti ena apulumutsidwe ndi kupita Kumwamba kwa muyaya, ndi kuthawa moto wosatha ku Gahena! Ngakhale atakuphani mwankhanza, ndikudziwa kuti ntchito ya Mulungu imene munakhanzikitsa idzapitirira kulalikira uthenga wabwino wosatha! Satana sangaleketse ntchito ya Mulungu yoonadi! Ngakhale muli m'ndende, Uthenga Wabwino udakali kulalikidwa mwamphamvu kuposa kale kudzera m'mabuku anu, ndi kudzera mwa Akhristu odzipereka amene ali ngati inu, Abusa, padziko lonse lapansi. Satana ndi mdani wogonjetsedwa. Ulemerero kwa Mulungu!

Vatican, hule wamkulu, sanasinthe ndipo sadzatero! Ndikupemphera kuti Mulungu asunge M'busa Alamo ku chirombo cha usatanachi ndipo ndikudziwa kuti Iye atero! "Palibe chida chosulidwira iwe chidzapindula." Lonjezo limenelo! "Musakhudze odzodzedwa Anga ndi kusapweteka Anga aneneri." Chivumbulutso 18:24 akuti, "Ndipo mwa iye [Vatican] munapezedwa mwazi wa aneneri ndi woyera mtima ndi onse amene anaphedwa padziko lapansi." Koma tikudziwa amene amapambana pa mapeto ndipo si mdierekezi! Pitirizani kupita patsogolo! Ndikudziwa kuti mutero, mpingo, ndi Tony. Monga Tony anati, "Ndikhulupilira munamva za lamulo la chidani latsopano—ngati mutsutsana ndi kukwatirana amuna kapena akazi okhaokha, kungakhale kulakwira lamulo." Ndikhulupilira alionetsetsa posachedwapa.

Zikomonso chifukwa cha zonse. Ndiyembekezera mabuku kuti ndizitsutsabe Satana! Ambuye alemekezeke!

W. D. Lakewood, CA

ndi chilungamo padziko lonse ['Inu muli ochokera mwa atate wanu mdierekezi, ndipo zolakalaka zake za atate wanu mufuna kuchita. Iye anali wakupha kuyambira pachiyambi, ndipo sanakhale mu choonadi, pakuti mulibe choonadi mwa iye. Pamene alankhula bodza, alankhula za mwini wake: pakuti ali wabodza, ndi atate wake' (Yohane 8:44).]. Masomphenya a Papa akukhazikitsira World Government ndi New World Order siakuti akhanzikitse mphamvu zambiri zatsopano, koma nthambi yolamulira yatsopano [imene ndi ya dziko loipa, losapulumutsidwa (koma kupulumutsidwa kwa anthu oyera)] yotumikira anthu (andale a mphulupulu) amene ali ndi udindo wolamulira, wokwanitsa kuweruza, ndi wodziwa kulangiza. Papa ananena kuti 'Nthambi tasankhayi (World Government) sidzakhala yamphamvu kwambiri, idzakhala m'manja mwa anthu ochepa, yomwe izilamulira anthu onse, nkumawadyera masuku pamutu ofooketsetsa.' [Izi ndi zenizeni zimene iwo akukonza kuti achite ndiponso akuchita.] Papa anafotokozanso masomphenya ake kuti ndi 'mphamvu [yoipa] ya chikhalidwe' kapena ulamuliro wa chikhalidwe [ngati ali ndi khalidwe kwambiri, n'chifukwa chiyani boma ili sililola Malamulo Khumi m'masukulu a boma kapena m'nyumba za boma, monga m'makhothi?] zimene zili ndi 'mphamvu yosintha molingana ndi chifukwa, monga kuti, ulamuliro wa kutenga nawo mbali, kuchepetsedwa ndi lamulo m'mathero ake a lamulo.'"[19]

MULUNGU amatiuza tonse kukhala kutali ndi mabungwe a Satana, makamaka One World Government ya Satana, imene inapatsidwa ulamuliro wake kuchokera kwa Satana pamwamba pa New World Order.[20] Kodi inu mukukhulupirira MULUNGU, kapena mwambo wa Vatican Roma Katolika ndi Papa a uSatanawa? Palibe phindu mu kukhulupirira Papa wa Satana. Mapeto a iwo amene amakhulupirira ndi kumutsatira iye ndi muyaya mu Nyanja ya Moto.

Khulupirirani MULUNGU amene amanena mosapita m'mbali kuti palibe moyo pa pulaneti ina iliyonse. Komanso khulupirirani kuti maUFO ndi angelo ochokera Kumwamba, Alonda, ndipo khulupirirani MULUNGU WAMPHAMVU ZONSE, kachikenanso, amene amakhala paliponse, kutanthauza IYE ALI paliponse nthawi yomweyo.

*(Yapitirira patsamba 8)*

**19** http://www.activistpost.com/2012/12/vatican-calls-for-world-government-and.html **20** 2 Akor. 6:14-18, 2 Atesa. 2:3-12, Chiv. 2:18-25, 14:8-11, 16:1-2, 10-11, chap.17, 18:1-8, 19:1-3, 17-21, 20:4, 10

## Umboni wa Suzette Brown

Dzina langa ndine Suzette Brown ndipo ndakhala membala wa Tony Alamo Christian Ministries kwa zaka pafupifupi zisanu. Izi zakhala zaka zisanu zabwino koposa pa moyo wanga. Kudzera mu chiphunzitso cha m'busa wanga, Tony Alamo, ndadziwa kupemphera ndi kumugwiritsitsa Ambuye, mmene ndingawerengere Baibulo mwa uzimu ndi kuperekera umboni kwa anthu. Ndili othokoza kwambiri kwa Tony Alamo Christian Ministries chifukwa nditalandira chipulumutso, ndinkafuna kutumikira Ambuye ndi mtima wanga onse ndi kumpatsa Iye moyo wanga, ndipo zitseko za tchalitchi chimenechi zinanditsekukira.

Ndinaleledwa m'mipingo ya Chikhristu yosiyanasiyana kuchokera mmene ndinali wa chichepele. Ndinkakonda nyimbo za uzimu mmene ndinali wa mng'ono. Amalume anga a Mike anali m'busa ndipo anandiuzapo za Gahena osatha pamene ndinali wa zaka zisanu. Anandiuzapo za moto ndi mazunzo amuyaya. Ndinawafunsa, "Kodi ndingapulumutsidwe bwanji?" Anapemphera nane. Ndikukumbukira kupemphera, "Ambuye, ndikhulupilira munafa pamtanda chifukwa cha machimo anga ndipo munaukanso tsiku la chitatu. Lowani mumtima mwanga Ambuye Yesu." Sanandiuzepo za mphamvu ya mwazi wa Yesu potsuka machimo anga kapena kuti ndizisunga malamulo khumi a Mulungu. Amalume anga anandiuza ndapulumutsidwa ndipo sindidzataya chipulumutso changa. Ndinakhulupirira kuti, "ukangopulumutsidwa, udzakhala opulumutsidwa nthawi zonse," ndipo kuti palibe olungama. Izi ndizomwe matchalitchi anandiuza. Ndinkaganiza kuti chomwe chinkafunika kuti ndilandire cha chipulumutso ndikunena pemphero ndi kukhulupilira kuti Yesu anafa pa mtanda chifukwa cha machimo anga. Kuyambira nthawi imene ndinali ndi zaka zisanu ndinkakhulupilira kuti ndinapulumutsidwa.

Ndili wamkulu ku sukulu ya sekondale, ndinkapita ku Southern Baptist Church. Abusa ndi m'tsogoleri wa kwaya ankachita za uchimo zomwe zinandipangisa kubwelera m'mbuyo ndi Chikhristu. Osati chifukwa ndinali wa bwino, nanenso ndinali wochimwa. Ndinasiya kupita ku tchalitchi.

Chaka changa chomaliza ku sukulu ya sekondale, ndinkafuna kusangalala ndi kukhala okondwa. Ndinali ophunzira wa nzeru kwambiri (straight A). Ndinayamba kuyenda ndi magulu olakwika chaka changa chomaliza ku sukulu ya sekondale ndipo ndinayamba kugwiritsa ntchito makhwala ozunguza bongo (methamphetamine). Ndinkapanga izi tsiku lili lonse. Ndinapezeka ndayamba kunama, kuba ndi kugulitsa mankhwala ozunguza bongo. Moyo wanga unasokonekera. Ndinakhala osochera ndi okhumudwa. Ndinakhala opanda pake ndi osowa m'bale. Ndinachoka kunyumba ndinakakhala ndi chibwenzi changa chomwe chinkagulitsa makhwala ozunguza bongo ndipo sindinali osangalala. Ndinasiya koleji komanso ndinasiya ntchito ndipo ndinakakhala moyo wa mankhwala ozunguza bongo. Ndinachita izi kwa zaka 8 za moyo wanga. Sindinkafuna kukhala opulukira, koma Satana anandigwiritsa ntchito ndipo sindinkatha kusintha.



*Sister Suzette Brown*

Patapita zaka zingapo chichitikireni zomwe zinachitika pa 11 September, ndinaona, "Loose Change." Ndinawona ma Twin Tower akugwa ndipo ndinadziwa kuti chinali chigumulo chochita kukonzedwa. Ndinayamba kuchita kafukufuku wa zomwe zinachitika pa 11 September. Ndinkafuna kudziwa zoona zenizeni, yemwe ankakhudzidwa ndi zomwe zinachitika pa 11 Sep-

*(Yapitirira patsamba 6)*

## Umboni wa Suzette Brown

*(Yachokera patsamba 5)*

tember. Sindinkalikhulupilira boma lathu. Ndinapanga kafukufuku kwa zaka 4 mpaka 5—maola masauzande ambirimbiri akafukufuku. Kafukufukuyu anali ngati kuthawa moyo omwe ndinkachita ndipo ndinangozolowera. Nthawi imeneyi m'moyo wanga, ndimatha kugwiritsa ntchito makhwala ozunguza bongo komanso kumapanga kafukufuku. Tsiku lina ndinadziwa kuti zomwe ndinkawerenga zinali zabodza. Ndinakhala pa kompyuta yanga ndikuyamba kupemphera, "Ambuye, ndionetsereni zoona zake za pa 11 September; ndikufunitsitsa kudziwa zoona zake. Ndapanga kafukufuku yenseyi. Ndionetsereni zoona zake ndipo ikani bodza poyera." Ambuye pomwepo anandiyankha. Ndinayamba kupeza nkhani zokhudza ma Jesuits ndi Vatican. Sindinkadziwa kalikonse kokhudza Tchalitchi cha Katolika. Ndinawonera vidiyo pa Intaneti ya Alberto Rivera (wansembe wakale wa Jesuit) akuyankhula ku Tony Alamo Christian Ministries mu 1984. Ndinalemba pa ka pepala komata ka yelo, "Tony Alamo Christian Ministries" ndipo ndinayika pambali, kuyiwaliratu za Tony Alamo Christian Ministries. Ndinapitiliza kupanga kafukufuku wa ma Jesuit ndi Vatican. Ndinkakhulupilira za mkwatulo chisautso chisanafike, kotero ndinaganiza sindikanapezeka pano pamene dziko la boma limodzi likadakhalapo. Mulungu anayamba kundizindikiritsa kuti tili m'masiku omaliza ndipo kuti Vatican ndi Make wa Zoipa. Sindinafune kukhulupilira.

Pa nthawi imeneyi, bwenzi langa linabwera tsiku lina ndikundiuza kuti za mkwatulo zinali za bodza. Ndinakwiya, koma sindinkadziwa Baibulo ndipo sindinathe kumuuza chili chonse cha m'Baibulo choperekera umboni pa chikhulupiliro changa. Kotero, ndinayamba kuwerenga Baibulo kuti ndipeze umboni otsutsana naye. Sindinapeze chili chonse mu Baibulo choperekera umboni otsusana naye. Ndinawerenga Mateyu chaputala 24 mavesi 29-30: "Chisautso cha masiku amenewo chikadzatha dzuwa lidzachita mdima, ndipo mwezi sudzapeleka kuwala kwake, ndipo nyenyezi zidzagwa kuchoka kumwamba, ndipo mphamvu zakumwamba zidzagwedezeka: Ndipo pamenepo chizindikiro cha Mwana wa Munthu chidzaonekera Kumwamba ndipo mitundu yonse ya padziko lapansi idzadziguguda pa chifuwa, nidzapenya Mwana wa Munthu ali nkudza m'mitambo ya kumwamba ndi mphamvu ndi ulemerero waukulu." Ndinaganiza, "Ambuye akubwera pambuyo pa msautso, osati usanachitike!" Komanso ndinapitiliza kuwerenga malembo oyera pomwe Iye ankawauza ophunzira Ake kuti "penyani," ndi "kukhala okonzeka," "simukudziwa za nthawi, mphindi kapena ola la kudza Kwanga." Ndinafunsa Ambuye, "Ndichifukwa chiyani Inu mukuwauza ophunzira Anu kupenya ndi kukhala okonzeka ngati sitingathe kutaya chipulumutso chathu? Ndi chiyani chomwe tikuyang'anira?" Ambuye analankhula kwa mtima wanga ndipo anati kwa ine, "Chifukwa ukhonza kutaya chipulumutso chako." Ndinakwiya kwambiri ndi matchalitchi. Ndinanamizidwa ndi kunyengedwa. Sindinafunenso kupita ku tchalitchi.

Pa nthawi imeneyi, ndinali otayikabe ndi okufa m'machimo anga, wachizolowezi chogwiritsa ntchito mankhwala ozunguza bongo. Ndinasiya kupanga kafukufuku wa maJesuit chifukwa ndinayamba kuchita mantha. Ndinkafuna nditaziyiwala. Tsiku lina, nditaledzera ndi mankhwala ozunguza bongo ndinali pa balaza ndipo ndinamva kumangika ndi kudzitsutsa mumtima mwanga kwambiri. Ndinamva mphamvu ya Ambuye ili pafupi nane. Ndinayamba kulira

## Germany

Okondeka M'busa Alamo,

Moni mu dzina la Ambuye. Ndinadalitsika powerenga webusaiti yanu. Ndimafuna ndipemphe ngati munganditumizire mabuku anu a m'Chingelezi ndi a m'Chijeremani. Zingakhale bwino ngati mungatumize okwana anthu 100 chifukwa ndikufuna aliyense m'tchalitchi mwanga akhale ndi bukhu *la Mesiya*. Chonde mungatitumizireko 50 a m'Chijeremani ndinso 50 a m'Chingelezi chonde. Komanso tikufuna ma Baibulo 10 a Chingerezi kapena Chijeremani ndipo tikufunanso timapepala togawa tokwanira anthu 1000 chifukwa tikufuna tikafikire anthu! Mulungu akudalitseni kwambiri pamene mukutithandiza kufikira otayika ndi mau a Mulungu! Tikuyembekezera kumva kuchoka kwa inu posachedwa!

Wanu mwa Ambuye,
Andre J. Schoen — Cologne, Germany

## South Africa

Ndiwabwino bwanji Iye, Mulungu wa Yakobo ndiponso Mulungu Woyera Wamoyo! Ndimathokoza Mulungu nthawi zonse, chifukwa utumiki wanu ukubweretsa anthu kwa Mulungu, ndipo amayamba kutumikira Mulungu ndi mtima wonse, maganizo onse, moyo wonse ndi mphamvu zonse. Zikomo, Abusa Tony Alamo. Chisomo ndi chifundo cha Mulungu chikhale ndi inu ndi mpingo wanu.

Gift Limban Nangwale — Johannesburg, Republic of South Africa

## Uganda

Okondeka M'busa Tony Alamo,

Moni kwa inu m'dzina la Yesu Khristu wathu. Ine ndine M'busa Embwata Yamungu, ogawa mabuku anu ku Kampala, Uganda.

Ndikufuna ndithokoze Mulungu chifukwa cha ntchito imene Iye anachita kudzera mu mabuku anu. Ndinagawa mabuku anu ku City Center College School ndiponso Nakivubo Primary School. Ophunzira oposa makumi atatu anapulumutsidwa. Ku Democratic Republic Of Congo, anthu khumi ndi asanu anapulumutsidwa.

Ndikupempha kuti munditumizire mabuku komanso ma Baibulo a Chingelezi makumi awiri, ma Baibulo a Chifaransa makumi awiri, mabuku a *Mesiya* a Chifaransa makumi awiri, mabuku a *Mesiya* a Chingelezi makumi awiri, matisheti makumi awiri ndi asanu a timu yaku Uganda ndi Congo. Ma Baibulo amenewo adzagawidwa kwa anthu amene angobadwanso mwatsopano, okondeka.

Wanu mwa Khristu,
M'busa Embwata Yamungu
Kampala, Uganda

mosatonthozeka. Ndinagwada pansi pa maondo anga ndikulilira kwa Ambuye ndi mtima wanga wonse, ndipo ndinati "Ambuye, ndinganene bwanji kuti ndimakukondani pamene ndikupitilizabe kuchimwa, ndipo ndingadzitchule bwanji m'Khristu pamene ndikupitilizabe kuchimwa?" Mtima wanga unasweka m'ziduswa 1 miliyoni. Ndinali wa manyazi, wosweka, ndi wonyasa kwambiri. Ambuye anandionetsera kuti sindinali opulumutsidwa ndipo kuti ndinali pa ulendo wa ku Gahena. Ndinafunsa Ambuye kuti andionetse njira yomwe ndingakonze kuti ndiyanjane Naye, kwinakwake ndingapite. Ndinauza Ambuye kuti ma tchalitchi onse anandinamiza ndipo kuyenera kuti kulipo komwe ndingapite. Sindinkafuna kupita ku Gahena, sindinafunenso kupitiriza kugwiritsa ntchito mankhwala ozunguza bongo, koma ndinkalephera kusiya. Sindinkafuna kupitiriza kuchimwa, koma ndinkalephera kusiya.

Ndinapeza kolembedwa komata ka yelo komwe ndinakalemba miyezi yapitayo, "Tony Alamo Christian Ministries." Ndinapita pa intaneti ndikuyamba kuwerenga zolembedwa za uthenga wabwino. Sanandikwanire. Malemba anali odzadzidwa ndi Mzimu Woyera ndipo anali ngati madzi amachiritso ku moyo wanga wosweka. Ndinawerenga malemba usana ndi usiku onse. Anali a mphamvu kwambiri. Ndinawerenga "Zinsisi za Papa," Nthambi zoipa za Dziko la Boma Limodzi Zoyima ngati Nthambi za United States," ndi "doko lina la ngale (pearl harbour)" ndipo ndinkadziwa kuti m'busa wathu ankadziwa choonadi.

Bwenzi langa anandiyendetsa kuchokera ku dera la San Francisco Bay Loweluka usiku. Ndinabwera ku mapemphero awiri la Mulungu. Ndinkamva mphamvu ya Mzimu Woyera. Ndinadziwa awa anali malo omwe Ambuye ankandifuna, koma ndinali ndisanakonzeke. Ndinapita kunyumba ndipo Ambuye anachita nane kwa masabata atatu. Ndinkakakamila mankhwala ozunguza bongo ndi bwenzi langa. Tsiku lina ndinkawerenga zolemba zanu mutu wake, "Njira yaku Mphamvu" ndipo ndinalandira chikhulupiliro chondiyika pamaondo anga. Satana ankandiuza kuti ndidzabwereranso ku mankhwala ozunguza bongo ndipo sindinafune kunena pemphero la ochimwa. Koma nthawi iyi maunyolo anali atamasulidwa. Ndinakhulupilira ndi mtima wanga wonse kuti Ambuye andimasula ku machimo anga komanso ku kukonda mankhwala ozunguza bongo. Ndinanena pemphero la ochimwa ndi mtima wanga wonse, ndikuchikhanzikitsa m'maganizo anga, "Ndidzatumikira Ambuye ndi mtima wanga wonse ndipo sindidzabweleranso ku moyo wa machimo." Ndinali pa maondo anga mu chipinda cha hotelo. Yesu Khristu anandimasula. Ndinadziwa ndapulumutsidwa. Ndinamva Mzimu Wake Woyera ukulowa mu mtima mwanga ndipo mwazi Wake ukutsuka machimo anga. Ndinali wosangalala. Ndinkalira misonzi ya chimwemwe. Ndinafuna kuthamanga kukauza aliyense za zomwe zandichitikira. Ndinalibe chilakolako chochita za mankhwala ozunguza bongo ndi kuchita za uchimo. Zokhazo zomwe ndinafuna kuchita ndi kuwerenga Baibulo ndi kutumikira Ambuye. Ndinalowa utumiki umenewu patapita masiku awiri nditawomboredwa pa 11 January, 2008. Ndinalongedza ma sutikesi awiri ndikukwera sitima ya pamtunda ndikubwera kuno. Sindinakhalepo okondwa kwambiri. Sindikugwiritsabe mankhwala ozunguza bongo. Ndinalandira Ubatizo wa Mzimu Woyera ndipo umu ndi mmene ndikufuna kuchitira moyo wanga wonse, kubwenzera kwa Ambuye chifukwa anapereka moyo Wake pa Kavari chifukwa cha ine. Ambuye zoonadi atha kukupulumutsa ndi kukupatsa mphamvu zogonjetsera tchimo. Anandichitira ine ndipo atha kuchitira wina aliyense amene ayitanira pa Iye ndi mtima wokhulupirika, ndi wolapa.



*M'bale Joseph Banda kugawa zolemba zokopa miyoyo za M'busa Alamo ku Chipata town center—Chipata, Zambia*

## Florida

Zikomo kwambiri! M'dziwitseni M'busa Alamo kuti ndapanga dawunilodi ndi kuika pa maCD mauthenga ake ambiri kuti azimveredwa. Akundipangitsa kusiya kumamvera wailesi (Ndinasiya kale TV yanga m'chaka cha 2003). Ndakhala ndikumvetsera mauthenga a M'busa Alamo nthawi zonse, ndipo ndikuphunzira zambiri za MAWU. Andidalitsa kwambiri!
Chikondi mu Yahshua,
Hank Christen
St. Petersburg, Florida

## Philippines

Wokondedwa Mlaliki Tony Alamo,

Ndikulemba izi mothandizidwa ndi mwana wa bwana wanga amene ali ngati mlongo wanga wamng'ono, chifukwa sindimatha kwenikweni kulemba mu Chingelezi ndi kuchilankhula. Ndili ndi zaka 19; ndinamaliza maphunziro a sekondale kuchokera ku limodzi mwa maboma a Philippines lotchedwa Antique ndipo ndinalembedwa ntchito ya m'nyumba ku banja labwinoli koposa chaka chimodzi tsopano.

Banjali limamvetsera porogaramu yanu pawailesi "Mautumiki a Tony Alamo" Lamulungu lililonse ndipo anali iwo amene anandilimbikitsa kuti nanenso kuzimvetsera. Nthawi zina sindimamvetsa chifukwa cha mawu ake, koma ndi thandizo lawo amandifotokozera zimene zikunenedwa mu pulogalamu yanu, ndipo ndikadziwa chimene akunena ndimayamba kuganizira za uthenga ndi kuuyamikira kwambiri.

Ndikhulupilira mupitiriza kufalitsa chikondi cha Mulungu kudzera mu porogaramu yanu. Mphamvu zambiri kwa inu ndipo chonde mundiike mu zolinga za pemphero lanu, makamaka thanzi la banja langa. Chonde mu zolinga za mapemphero anu muikemo banja limene ndikugwirako ntchito. Akhala akundichitira zabwino ndipo amanditenga ngati m'modzi wawo.
Salamat po (zikomo).
Liezzle Esponilla
Quezon City, Philippines

## MAGARETA A MOTO

*(Yachokera patsamba 5)*

Ngati chisankho chanu chili MULUNGU, ndiye nenani pemphero ili. Ndipo batizidwani, kulowetsedwa kwathunthu m'madzi, m'dzina la ATATE, MWANA, ndi la MZIMU WOYERA.[21] Phunzirani Baibulo la King James Version, ndi kuchita zimene likunena.[22]

**AMBUYE wanga komanso MULUNGU wanga, ndichitireni chifundo ndine munthu wochimwa.[23] Ndikukhulupirira kuti YESU KHRISTU ndi MWANA wa MULUNGU wamoyo.[24] Ndimakhulupiriranso kuti IYE anafera pamtanda ndipo anakhetsa mwazi WAKE wamtengo wapatali ndi cholinga choti machimo anga onse akhululukidwe.[25] Ndikukhulupiriranso kuti MULUNGU anaukitsa YESU kwa akufa pogwiritsa ntchito mphamvu ya MZIMU WOYERA,[26] ndiponso kuti IYE anakhala kudzanja lamanja la MULUNGU ndipo panopa akumva pemphero langa lolapali.[27] Ndikutsegula zitseko za mtima wanga, ndipo ndikukuyitanani kuti mulowe mumtima mwanga, inu AMBUYE YESU.[28] Tsukani machimo anga ambirimbiri achoke onse mu mwazi wamtengo wapatali umene INU munakhetsa m'malo mwanga pamtanda wa ku Kavari.[29] Ndikudziwa kuti mundimvera pemphero langali AMBUYE YESU; INU mukhululukira machimo anga ndi kupulumutsa moyo wanga. Ndikudziwa izi chifukwa MAWU ANU, Baibulo, limanena zimenezi.[30] MAWU ANU amati INUYO simudzakana kumvetsera pemphero la munthu aliyense, ndipo ine ndili m'gulu la anthu amenewo.[31] Choncho, ndikudziwa kuti INUYO mukundimvetsera pamene ndikupemphera ndipo ndikudziwanso kuti INUYO mundiyankha komanso mundipulumutsa.[32] Ndipo ndikukuthokozani AMBUYE YESU, chifukwa chopulumutsa moyo wanga, ndipo ndisonyeza kuyamikira mwa kuchita zinthu zimene INUYO munalamula komanso kupewa kuchita uchimo.[33]**

Pambuyo pa chipulumutso, YESU ananena kuti munthu ayenera kubatizidwa pomizidwa thupi lonse m'madzi, m'dzina la ATATE, ndi la MWANA, ndi la MZIMU WOYERA.[34] Muziphunzira mwakhama Baibulo la *Buku Lopatulika Ndilo Mau a Mulungu,* [King James Version] ndipo muzichita zimene Baibulolo limanena.[35]

AMBUYE akufuna kuti inuyo muziwuza ena za chipulumutso chanu. Mungathe kukhala wofalitsa uthenga wabwino wa M'busa Tony Alamo. Tizikutumizirani mabuku mwaulere. Imbani foni kapena tumizani imelo kwa ife kuti mudziwe zambiri. Tikukupemphani kuti muwuzeko ena uthengawu.

Ngati mukufuna kuti dziko lipulumutsidwe monga m'mene YESU akulamulira, mukufunika kupereka chakhumi kwa MULUNGU. MULUNGU anati, "Kodi munthu angabere MULUNGU? Inde, mwandibera kale. Koma akuti, Ife tikumubera bwanji MULUNGU? Mu chakhumi ndi mu zopereka. Anthuwo ndi otembereredwa chifukwa akundibera, ngakhale mtundu wonsewu [dziko lonse lapansi]. Bweretsani nonse chakhumi ['chakhumi' ndi gawo limodzi la magawo khumi (10%) ya malipiro anu] m'nkhokwe zanga n'cholinga choti pakhale nyama [chakudya cha Uzimu] mu nyumba YANGA [anthu opulumutsidwa] kuti mundiyese, akutero AMBUYE wa MAKAMU, kuti muone ngati sindidzakutsegulirani mazenera a Kumwamba ndi kukukhuthulirani madalitso amene mudzasowa malo owalandirira." Ndipo ndidzadzudzula anthu okudyerani masuku pamutu ndipo sadzawononga zipatso za nthaka yanu; ngakhalenso mphesa wanu sudzalephera kubala zipatso pa nyengo yake m'minda yanu, watero AMBUYE wa MAKAMU. Ndipo mitundu yonse idzakutchani odala: chifukwa dziko lanu lidzakhala labwino, watero AMBUYE wa MAKAMU" (Malaki 3:8-12).

**21** Mat. 28:19-20, Yoh. 3:5, Mach. 2:38, 19:3-5 **22** 2 Tim. 2:15, 3:14-17, Yak. 1:22-25, Chiv. 3:18 **23** Sal. 51:5, Aro. 3:10-12, 23 **24** Mat. 26:63-64, 27:54, Luka 1:30-33, Yoh. 9:35-37, Aro. 1:3-4 **25** Mac. 4:12, 20:28, Aro. 3:25, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 5:9 **26** Sal. 16:9-10, Mat. 28:5-7, Marko 16:9, 12, 14, Yoh. 2:19, 21, 10:17-18, 11:25, Mac. 2:24, 3:15, Aro. 8:11, 1 Akor. 15:3-7 **27** Luka 22:69, Mac. 2:25-36, Aheb. 10:12-13 **28** 1 Akor. 3:16, Chiv. 3:20 **29** Aef. 2:13-22, Aheb. 9:22, 13:12, 20-21, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 1:5, 7:14 **30** Mat. 26:28, Mac. 2:21, 4:12, Aef. 1:7, Akol. 1:14 **31** Mat. 21:22, Yoh. 6:35, 37-40, Aro. 10:13 **32** Aheb. 11:6 **33** Yoh. 5:14, 8:11, Aro. 6:4, 1 Akor. 15:10, Chiv. 7:14, 22:14 **34** Mat. 28:18-20, Yoh. 3:5, Mac. 2:38, 19:3-5 **35** Deut. 4:29, 13:4, 26:16, Yos. 1:8, 22:5, 2 Tim. 2:15, 3:14-17, Yak. 1:22-25, Chiv. 3:18

***Ngati mukufuna kudziwa zambiri kapena ngati mukufuna mabuku kapenanso nkhani zina zimene zimakusangalatsani, tiimbireni foni kapena tilembereni.***

**Tony Alamo, World Pastor, Tony Alamo Christian Ministries Worldwide • P.O. Box 2948, Hollywood, CA 90078**
**Lamya ya pemphero ndi uthenga maola 24: +1 (661) 252-5686 • Fax +1 (661) 252-4362**
**www.alamoministries.com • info@alamoministries.com**

*Tony Alamo Christian Ministries Worldwide imalandira anthu onse ndipo imapereka zinthu zofunika Kwa onse amene ali ku U.S. amene akufunitsitsadi kuti ayambe kutumikira AMBUYE ndi mtima wawo wonse moyo wawo wonse ndi mphamvu zawo zonse*

**Mapemphero amachitika usiku uli wonse nthawi ya 8 Koloko usiku ndi Lamulungu nthawi ya 3 Koloko madzulo ndiponso 8 Koloko usiku ku Tchalitchi cha kudera la Los Angeles: 13136 Sierra Hwy., Santa Clarita, CA 91390, +1 (661) 251-9424**

**Magalimoto a ulere opita ndi kuchokera ku mapemphero amaperekedwa pa kona ya Hollywood Blvd. ndi Highland Ave., Hollywood, CA tsiku lili lonse nthawi ya 6:30 madzulo, Lamulungu lili lonse nthawi ya 1:30 madzulo ndi 6:30 usiku.**

**Mapemphero amachitika mu Mzinda wa New York Lachiwiri lili lonse nthawi ya 8 Koloko usiku ndi madera ena usiku okhaokha. Chonde imbani foni kuti mumve zambiri: +1 (908) 937-5723. ZAKUDYA ZIMAGAWIDWA PA MAPETO PA MAPEMPHERO ALI WONSE**

**Funsani buku la M'busa Alamo, lakuti *Mesiya,* losonyeza KHRISTU kuyambira ku Chipangano Chakale mu maulosi oposa 333.**

*Khalani wogwira ntchito yokolola miyoyo ya anthu pakukhala ogawira mabuku a M'busa Alamo*
*Mabuku ndi zinthu zonse zomvetsera n'zaulere, ndipo simulipira ndalama yotumizira*
*Ngati wina akukuuzani kuti mupereke ndalama pa zinthu zimenezi, chonde imbani pa +1(661) 252-5686.*

**M'BUKU ILI MULI CHIKONZERO CHENICHENI CHA CHIPULUMUTSO (Machitidwe 4:12).**
**MUSALITAYE, PATSANI ENA KUTI AWERENGE.**

**Anthu amene muli m'mayiko ena, tikukulimbikitsani kuti mumasulire n'chinenero chanu mabukuwa. Ngati mukusindikizanso bukuli, musaiwale kuika mawu ali m'munsiwa omwe ndi okhudzana ndi zamalamulo:**

© Copyright February 2013, 2015 All rights reserved World Pastor Tony Alamo ® Registered February 2013, 2015